Zimene Mungachite Kuti Mulungu Apitirize Kukukondani (Gawo 1)

Zoti muchitezi zachokera m'mutu 19 wa buku lakuti *Kodi Baibulo Limaphunzitsa Chiyani Kwenikweni?* lomwe likupezeka pa jw.org/ny.

ZIMENE MUYENERA KUCHITA: Ganizirani mofatsa zimene mumakhulupirira komanso chifukwa chake mumazikhulupirira, fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa, komanso onani mmene mungafotokozere zimene mumakhulupirira kwa anthu ena.

KODI KUKONDA MULUNGU KUMATANTHAUZA CHIYANI?

1 GANIZIRANI MOFATSA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

Kodi anthu ena anganene chiyani?

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani?

N'chifukwa chiyani mumazikhulupirira?

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

Timakonda Mulungu chifukwa chakuti timayamikira zimene anatichitira.

(Onani mutu 19 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 1-5.)

Werengani Salimo 91:2.

Kodi Yehova amawachitira chiyani anthu omwe amamukhulupirira?

_____

_____

_____

Werengani Salimo 37:29; Yohane 3:16.

Kodi Yehova wasonyeza bwanji kuti amakukondani inuyo?

_____

_____

_____

Mtengo wabwino umabala zipatso zabwino. Nayenso munthu amene amakonda Mulungu amasonyeza chikondicho mwa zochita zake.—Mateyu 7:16-20.

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Tikamakonda Mulungu timasonyeza kuti tikuyamikira chikondi chimene amatisonyeza.

(Onani mutu 19 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 6-9.)

Werengani 1 Yohane 5:3.

Kodi timasonyeza bwanji kuti timakonda Mulungu?

Werengani Yesaya 48:17, 18.

Kodi timapindula bwanji tikamasonyeza kuti timakonda Mulungu pomumvera?

Kodi **inuyo** mwapindula bwanji chifukwa chomvera malamulo a Mulungu?

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

WINA AKANENA KUTI…

Mulungu amakonda anthu onse, mosaganizira zimene anthuwo amachita.

MUNGANENE KUTI…

Ndi zoona kuti Mulungu wasonyeza chikondi chachikulu kwa anthu onse. Koma ndikuganiza kuti zimene timachita zimakhudzanso mmene iye amationera chifukwa…

Kodi ndi lemba liti limene mungamuwerengere munthuyo?

Poganizira zimene munthuyo wanena, kodi mungalifotokoze bwanji lembalo?

WINA AKANENA KUTI…

Ndikuganiza kuti Mulungu amafuna kuti tizisiyanitsa zabwino ndi zoipa potengera mmene tikumvera.

MUNGANENE KUTI…

Ndi zoona kuti Mulungu anatipatsa chikumbumtima. Koma ndikukhulupiriranso kuti timafunikanso malangizo ochokera m’Baibulo chifukwa…

Kodi ndi lemba liti limene mungamuwerengere munthuyo?

Poganizira zimene munthuyo wanena, kodi mungalifotokoze bwanji lembalo?

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania